000095120 for more visit www.gcerevision.com

EXAMINATIONS COUNCIL OF ZAMBIA

GRADE SEVEN COMPOSITE EXAMINATION – 2016

# Cinyanja

SUBJECT 5/1 NTHAWI: MPHINDI 60

TD/NYA5/G7/2016

1 Werengani dongosolo la macitidwe a mayeso awa mwatsatane-tsatane ndi mosamala.

2 Musatsekule tsamba iri musanauzidwe kucita tero. Aphunzitsi anu adzakuuzani nthawi yotsekula pepalali kuti muyambe kuyankha mafunso.

3 Pepala iri liri ndi mafunso okwanira makumi asanu ndi limodzi (50) cabe mu zigawo zisanu ndi cimodzi. Muyankhe mafunso onse. Mukatsiriza kuyankha mafunso a m'cigawo cimodzi, musayembekezere kuuzidwa kuti mupite ku cigawo cina. Pitirizani kulemba mpaka kutsiriza mafunso onse.

4 Funso lirilonse liri ndi mayankho anai (4) amene limodzi cabe ndilo loyenera lopambana ena onse. Mukasankha yankho lanu, phimbani yankho lanulo pophimba mkombero muli yankho mwasankha motere.

CITSANZO: [A] [B] [■] [D]

Yankho lacitatu **'C'** ndilo lopambana onse. Conco phimbani yankho liri mu mkombero **'C'**.

Werengani malangizo ndi zitsanzo zonse ziri mcigawo ciriconse molingalira bwino ndiponso mosamala. Musanaphimbe yankho lanu muwerenge mayankho onse mosamala.

5 Ngati mufuna kusintha yankho mwasankha poyamba, fafanizani yankho loyamba mwaukhondo pogwiritsa nchito cofafanizira copanda dothi.

6 Musataye nthawi yaitali kufuna kuyankha mafunso obvuta. Mungabwerere ku mafunsowo potsirizira pake ngati kwakhala nthawi.

7 Ngati mwatsiriza kuyankha mafunso onse, kukatsala nthawi, gwiritsani nchito mphindi zotsalirazo kupititsamo mu mayankho anu. Onani kuti mwayankha **mafunso onse.**

8 Imikani manja anu tsopano ngati:

**(i)** muli ndi funso.

**(ii)** pepala lanu la mayankho siliri lolongosoka



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



## CIGAWO COYAMBA

### Malangizo

Funso lirilonse liyamba ndi ciganizo comwe ciri ndi liu kapena dera lina losowa m'malo amene aonetsedwa. Munsi mwake mudzapezamo mau kapena madera a ziganizo anai. Liu limodzi mwa mau anai ndilo litsiriza bwino ciganizo conse.

**Citsanzo:** Mnyamata aliyense ali ndi kakhasu ... kobzalira mtedza.

- **A** kanga
- **B** langa
- **C** kake
- **D** yake

Yankho "C" **kake,** ndilo liu litsiriza bwino ciganizo conse. Conco munakaphimba yankho "C" mu mkombero motere:

[A] [B] [■] [D]

**Tsopano yankhani mafunso otsatira:**

**1** Pa msonkhano wa azimai wacirezi kunabwera anthu...

- **A** acepa.
- **B** kocepa.
- **C** ocepa.
- **D** tocepa.

**2** Dzina ... ndine Malita, nanga iwe ndiwe ndani?

- **A** lake
- **B** lathu
- **C** langa
- **D** lanu

**3** ... dzina lake ndi Chimangeni Daka.

- **A** Ine
- **B** Inu
- **C** uyu
- **D** iwo

**4** Ine sindidzabwera kumsonkhano ... ndadwala malungo.

- **A** cifukwa
- **B** kapena
- **C** mwina
- **D** olo



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



5 Mnkhwere ndi dzina lina la nyama ya mthengo yomwe imachedwanso kuti...

- **A** mphaka.
- **B** mwanabere.
- **C** kambuku.
- **D** nyani.

6 Afakabelo akondedwa ndi anthu onse pamudzi pake cifukwa anali wa ...

- **A** Manyonzo.
- **B** mwano.
- **C** umbombo.
- **D** ulemu.

7 Nsapato yake ... yakuda inang'ambika dzulo.

- **A** ija
- **B** lija
- **C** tuja
- **D** zija

8 Daliyase analephera kukhoza mayeso cifukwa anali ...

- **A** waluntha.
- **B** wanzeru.
- **C** waulesi.
- **D** wocenjera.

9 Dera la Magwero ... ku Chipata.

- **A** apezeka
- **B** lipezeka
- **C** imapezeka
- **D** kapezeka

10 Yeremiya ayenda ... cifukwa analasidwa kuphazi ndi minga.

- **A** mofulumira
- **B** monyada
- **C** motang'adza
- **D** motsimphina

11 ....wobiriwira unapha Mbuzi.

- **A** Cilumbusha
- **B** Kasokolowe
- **C** Msipu
- **D** Nthudza



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



12 ...! yandiluma pa diso cenjere.

A Haaa
B Inee
C Mainee
D ooo

13 Atsikana a kumudzi ... .Galuwawo akonda kubvina cimtali.

A ku
B kwa
C pa
D wa

14 Kumsokhano wa zaulimi kunabwera anthu. ...

A wabiri.
B wocepa.
C yambiri.
D zambiri.

15 Buku ....liri pathebulo ndi langa.

A amene
B cimene
C imene
D limene

**CIGAWO CACIWIRI**

Cigawo ici ciri ndi mbali ziwiri .Mbali yoyamba iri ndi ziganizo zimene ziri mucindunji ndi mcisandunji(direct and indirect speech) Mbali yaciwiri iri ndi Mafunso pa zopumira. Yankhani mafunso kulingana ndi malangizo opezeka pambali iri yonse.

**A** Cindunji ndi cisandunji (direct and indirect speech) sankhani Ziganizo zimene zalembedwa moyenera mwaziganizo zopezeka pa mafunso **16** ndi **17**.

16 Sankhani ciganizo coyenera mwa ziganizo zotsatirazi.

A Zamene anena anthu awa ndi zoona.
B Zimene anena anthu awa ndi zoona.
C Zimene banena banthu aba ndi zoona.
D zimene wanena awa wanthu ndi zoona.

17 Sankhani ciganizo coyenera mwaizi zinai mwapatsidwa munsimu.

A "Ndidzakhoza mayeso anga," anatero Zilose.
B Ndidzakhoza mayeso anga"anatero Zilose"
C "Ndidzakhoza mayeso anga, anatero Zilose"
D "Ndidzakhoza mayeso anga anatero Zilose"



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



**ZOPUMIRA**

**MALANGIZO**

Mbali ya funso lirilonse liri ndi ciganizo comwe sicinaikidwe zopumira. M'malo onse amene mufunika zopumira mwaikidwa manambala. Munsi mwa ciganizo ciriconse mudzapezamo njira yosonyera kaikidwe ka zopumira m'malo muli munambala muja

**Citsanzo** kusukulu lero (1) taphunzira masamu ndi cinyanja cabe (2) Pamene takomboka (3) tinapita ku munda wa sukulu kukalima (4).

| | 1 | 2 | 3 | 4 |
|---|---|---|---|---|
| **A** | , | . | , | . |
| **B** | , | . | . | ? |
| **C** | , | ? | . | . |
| **D** | ! | . | ? | . |

Yankho '**A**' ndilo laikidwa zopumira muyenera. Conco munakaphimba yankho '**A**' mu mkombero motere:

■ [B] [C] [D]

**Tsopano yankhani mafunso otsatira awa:**

**18** Kodi mukupita kuti (1)ndaona nonse mutuluka mkalasi (2) kodi ndipite nanu (3) cifukwa ndi nthawi yopumula tsopano (4).

| | 1 | 2 | 3 | 4 |
|---|---|---|---|---|
| **A** | ? | . | ? | . |
| **B** | ? | . | ? | ? |
| **C** | , | , | , | ? |
| **D** | ? | ? | ? | . |

**19** Kodi mwana uyu alibe malaya ndi wa ndani(1)cifukwa ninji musunga ana tere (2) pitani mukamubvalike(3)muzisamala ana anu bwino(4)

| | 1 | 2 | 3 | 4 |
|---|---|---|---|---|
| **A** | ? | . | . | , |
| **B** | , | , | ? | ? |
| **C** | ? | ? | . | . |
| **D** | ! | . | . | ? |

**20** Patsiku lokumbukira ufulu wathu wodzilamulira(1)anthu ambiri amabvina(2) kumwa(3)kudya ndi kupembedza mulungu pa zomwe anawacitira(4)

| | 1 | 2 | 3 | 4 |
|---|---|---|---|---|
| **A** | . | , | , | . |
| **B** | ! | . | , | , |
| **C** | , | ! | . | . |
| **D** | , | , | , | . |



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



## CIGAWO CACITATU

### Malangizo

M'cigawo ici, funso lirilonse liri ndi ziganizo zinai zimene ziri ndi manambala osaikidwa mu mndandanda wabwino. Ikani ziganizo izi mu m'ndandanda wa dongosolo labwino kuti zonenedwa zonse zikhale zomveka.

Werengani ziganizo zonse mosamala ndi kusankha njira yolongosoka motsatira manambala kuti zikhale mudongosolo lomveka bwino.

**Citsanzo:** **1** kodi ndiwe munthu wa mtundu wanji

**2** sitidzayenda nawenso kuyambira lero

**3** wosafuna kudzisamalira?

**4** umangotic ititsa manyazi pagulu la atsikana

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 4 | 3 | 1 | 2 |
| **B** | 3 | 2 | 4 | 1 |
| **C** | 1 | 3 | 4 | 2 |
| **D** | 2 | 4 | 3 | 1 |

**Yankho "C"** ndilo lolongosoka mu mumndandanda. Nkhani yonse iyenera kukhala tere:

[ A ] [ B ] [redacted] [ D ]

**1** kodi ndiwe munthu wa mtundu wanji

**3** wosafuna kudzisamalira?

**4** umangoticititsa manyazi pagulu la atsikana.

**2** sitidzayenda nawenso kuyambira lero

**Tsopano yankhani mafunso awa:**

**21** Sankhani ciganizo colongosoka.

- **A** Mukanabwera dzulo, mukanandipeza.
- **B** Mukanabwera dzulo, mukanadzandipeza.
- **C** Munakabwera mailo,mukanipeza.
- **D** Munakabwera zulo, mudzandipeza.

**22** **1** Ndiponso ndi nyama yopanda mphamvu.

**2** Thupi lake ndi lalikulu ku mutu koma ndi locepa kumcira.

**3** Miyendo yake yakutsogolo ndi yaitali yakumbuyo ndi yaifupi

**4** Fisi ndi nyama yodabwitsa m'maonekedwe ake.

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 3 | 1 | 2 | 4 |
| **B** | 4 | 1 | 3 | 2 |
| **C** | 1 | 2 | 4 | 3 |
| **D** | 3 | 4 | 1 | 3 |



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



**23** **1** Umabisa zakudya zako
**2** bwanawe ndiwe wocenjera
**3** uyenera kusintha khalidwe lako
**4** zako umadya wekha.

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 2 | 3 | 1 | 4 |
| **B** | 3 | 2 | 1 | 4 |
| **C** | 4 | 1 | 2 | 3 |
| **D** | 2 | 1 | 4 | 3 |

**24** **1** Pambuyo paphunziro limenelo, Yona anakweza dzanja lake nafunsa aphunzitsi akewo funso lakuti.
**2** Tsiku lina ana a Giredi 7 amaphunzira za mbiri yakale ya Zambia.
**3** "Kodi a prezidenti woyamba a dziko la Zambia anali ndani?"
**4** Aphunzitsi anayankha nati, anali a prezidenti Kenneth David Kaunda.

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **A** | 2 | 1 | 4 | 3 |
| **B** | 1 | 2 | 3 | 4 |
| **C** | 3 | 4 | 1 | 2 |
| **D** | 2 | 1 | 3 | 4 |

**25** Sankhani ciganizo coyenera cimene cingapangidwe ndi mau awa, **cizimyalupsya** ya yoyamba ndiyo mvula.

**A** Ndiyo ya cizimyalupsya yoyamba mvula.
**B** Cizimyalupsya ndiyo mvula ya yoyamba.
**C** Mvula ya cizimyapsya ndiyo yoyamba.
**D** Yoyamba ndiyo cizimyalupsya ya mvula.

**CIGAWO CACINAI**

**Malangizo**

Mcigawo ici, mudzayesedwa ngati mungathe kudziwa matanthauzo a mau, madera a ziganizo kapena ziganizo zomwe. Munsi mwafunso lirilonse muli mayankho anai. Yankho limodzi cabe ndilo lopambana ena onse. Phimbani yankho mwasankha monga mwasonyezedwa pansipa.

**Citsanzo:** Tikati Belita **wapsa mtima** ndiko kuti • • •

**A** anatentha mtima.
**B** mtima wake unali pamoto.
**C** mtima wake unapsa ndi moto.
**D** wakalipa kwambiri.



for more visit www.gcerevision.com

 for more visit www.gcerevision.com

**Yankho "D"** ndilo loyenera.

[ A ] [ B ] [ C ] ■

**Tsopano yankhani mafunso awa:**

**26** Kumbuwa milomo ndiko kunena kuti...

- **A** njala
- **B** njazi
- **C** njiru
- **D** njuci

**27** Malingose ndi **kavuwevuwe.**Liu loti **kavuwevuwe** litanthanza...

- **A** kunena zabodza za anthu ena.
- **B** munthu wamtima wabwino.
- **C** munthu wodzisamala.
- **D** munthu wobvuwika nsima m'madzi.

**28** "**Cuma ndi mphepo**" manenedwewa atanthauza ciani?

- **A** Cuma cikudza ndi mphepo.
- **B** Cuma cimatha nthawi iriyonse.
- **C** Mphepo ndico cuma.
- **D** Pali mphepo ndipo pali cuma.

**29** **Cidakwa** sicimapatsidwa ulemu. Kodi **cidakwa** ndiko kuti ciani?

- **A** Munthu okhala yekha.
- **B** Munthu wokoka fodya kwambiri.
- **C** Munthu wakumwa mowa kwambiri.
- **D** Munthu wolakwira mnzake.

**30** Sankhani tanthauzo lolongosoka la mwambi woti" **nkhuyu zodya mwana zinapota mkulu** kucokera ku matanthauzo awa.

- **A** mwambi wocenjeza makolo kuti ayenera kulangiza ana awo.
- **B** mwambi wocenjeza makolo kuti ayenera kulangidwa pamodzi ndi ana awo.
- **C** mwambi wocenjeza makolo kuti ayenera kutamanda ana awo powalangiza.
- **D** mwambi wocenjeza makolo kuti sayenera kulangiza ana awo.

**31** Masiye ndi **wacibwana.**Liu **wacibwana** litanthanza...

- **A** kucita zinthu za masewera.
- **B** kucita zinthu za acikulire.
- **C** kucita zinthu zabwino.
- **D** kuctita zinthu zoopsya.



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



32 "**Kapinga udagwetsa amfumu**" ndiko kuti ciani?.

A Cingwe.

B Nthambo.

C Tulo.

D Udzu.

33 Tikanena kuti amai Mary Phiri ndi **acumba** titanthauza kuti ...

A mkazi wacidwi ndi anthu.

B mkazi wosabereka kapena wosabala.

C mwamuna wacidwi ndi anthu.

D mwamuna wosabereka kapena wosabala.

34 Ngati munthu wina ndi **waliuma**, ndiye kuti iye ndi ...

A wabwino mtima.

B womvera za anzake.

C wosamvera za anzake.

D wokongola thupi.

35 Tikati amai Chimtengo ndi **wonyang'wa** ndiye kuti iwo ndi ...

A wodekha.

B wolekerera.

C wonyada.

D wotopa.

## CIGAWO CACISANU

### MALANGIZO

Munsimu muli mau ndi ziganizo zolembedwa m'cingerezi sankhani yankho limene liri ndi liu kapena ciganizo cimene catembenuzidwa m'Cinyanja comveka bwino, mwa ziganizo zinai zapatsidwazi.

36 Liu la kuti "**farmer**" m'cingerezi ndi ...m'Cinyanja.

A mlimi

B msodzi

C mtsotsi

D munda

37 Cinganizo ca kuti **"It has rained today"**m'cingerezi ndi ...m'Cinyanja.

A Kwagwa mvula lero

B Mvula yagwa dzulo

C Mvula yinagwa lero

D Mvula yagwa masana



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



**38** Liu la kuti "**chief**" m'cingerezi ndi ...m'Cinyanja.

- **A** kaphaso
- **B** kapitao
- **C** mfumu
- **D** nduna

**39** Liu la kuti "**peace**" m'cingerezi ndi ...m'Cinyanja.

- **A** cipolowe
- **B** mtendere
- **C** nkhalwe
- **D** ufulu

**40** Liu la kuti "**dance**" m'cingerezi ndi ...m'Cinyanja.

- **A** bvina
- **B** sesema
- **C** lumpha
- **D** meka

**CIGAWO CACISANU NDI CIMODZI**

**Werengani nkhani iyi ndipo muyankhe mafunso otsatira.**

Tsiku lina nguluwe inayenda mtunda wautali motero kuti inamva ludzu. Mwamwayi inatulukira pa citsime ca nyama. Iyo siyinafune kugwiritsira nchito cotungira madzi cimene cinali pa citsimepo. Kotero kuti inaganizira zolumphiramo m'citsimeco. Italumphiramo **enaphadi ludzu lake**. Kenaka inaganizira zotuluka m'citsimeco koma inalephera cifukwa citsimeco cinali cakuya.

Mwadzidzi njati inatulukira pa citsimeco.Iyo poti **isunzire** mcitsimeco,inaona nguluwe iri kumwa madzi. Mosataya nthawi njati inafunsa nguluwe cimene inali kucita mcitsimemo. Poyankha nguluwe inati, inali kupha ludzu pakuti madzi yotunga siyanaliyokoma. Mauwa yanakopa mtima njati kotero kuti nayonso inalumphiramo. Itatha kupha ludzu inayesa kuti ituluke koma inalephera. Kenaka awiriwo mwamtima watapakale anapangana zoti nguluwe ikwere pamsana pa njati kuti ituluke ndikupatsa mtengo njati kuti nayonso ituluke. Nguluwe inatulukadi ndi kuthawa.

Patangopita masiku awiri njati inalefuka ndi njala m'citsimemo.Inalibenso ciyembekezo cakuti ingatuluke m'citsime muja. Patsikulo njati **inanongoneza bondo**. Iyo inakumbukira mkazi ndi ana ake niyiganiza kuti **siyidzawaonanso.**

**Tsopano yankhani mafunso yotsatira awa (41 – 50).**

**41** Njati inawonetsa kufooka patatha...

- **A** tsiku limodzi.
- **B** masiku awiri.
- **C** masiku atatu.
- **D** masiku anai.



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



**42** Kodi ndi nyama iti imene inayambirira kufika pacitsime?

**A** Bondo
**B** Ludzu
**C** Nguluwe
**D** Njati

**43** Nguluwe inalephera kutuluka m'citsime muja cifukwa cakuti...

**A** citsime cija cinali cakuya.
**B** citsime cija cinali cosazama.
**C** Iyo inalibe mphamvu zolumphira.
**D** Iyo inali yonenepa.

**44** Kodi ndi nyama iti ya m'mudzi imene imafanana ndi njati?

**A** Cona
**B** Galu
**C** Mbuzi
**D** Ng'ombe

**45** Mau akuti njati **inanong'oneza bondo** atanthauza kuti ...

**A** inadandaula kwambiri.
**B** inafuna kukambirana ndi njati.
**C** inafuna kuona banja lake.
**D** inafuna kuona njati.

**46** Kodi njati inali ndi ciyembekezo cotani m'citsime muja?

**A** Cosatuluka
**B** Cotuluka
**C** Comira
**D** Coyangalala

**47** Pamene njati inafika pacitsimeco inacita ciyani poyamba.

**A** idakambirana ndi ludzu.
**B** inakambirana ndi nguluwe.
**C** inatenga cotungira madzi.
**D** inasuzira mcitsime.

**48** Kodi ndiphunziro lotani limene titengamo mnkhaniyi? Tizicita zinthu...

**A** modziyenereza.
**B** moganizira zapatsogolo.
**C** mokomera ife tonkha.
**D** zolanga otilangiza



for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com



**49** Mutu woyenera nkhaniyi ndi ciani?

- **A** Citsime ca nyama
- **B** Dambo la nguluwe
- **C** Mtunda ndi ludzu
- **D** nguluwe ndi njati

**50** N'ciani cimene cinapangitsa nguluwe kuti ilumphire m'citsime? Iyo.

- **A** Inali italema kwambiri.
- **B** Inafuna kumwa madzi msanga.
- **C** Siinafune kutaya nthawi.
- **D** Siinacione cotungira madzi.

**MAYESO ANU ATHA**

for more visit www.gcerevision.com

for more visit www.gcerevision.com